ttb_Nya_0834_script

1 Atesalonika : 5:11-28

Mutu : Malamulo ya a Khristu

Landirani moni wa Kumwamba inu wokondedwa anzanga apaulendo. Lero Ambuye afuna atitsogoze ndi mau apa Filemoni 17, amene akunena kuti, "Ngati tsono undiyesawoyanjananawe, umlandire iye monga ine mwini. Koma ngati anakulakwira kanthu, kapena wokongola kanthu, undiwerengere ine kameneko."

Tsono mupologalamu yatha tinali kusanthula 1 Atesalonika 5:1-11, momwe timakambirana za chiyembekezo cha kubwera kwa Kristu kuti ndicho chifulumize wokhulupirira kumtumikira Kristu. Ndipo lero pa 1 Atesalonika 5:11-28, tiona za malamulo ya akristu.

Mu verse 11, tidaona kuti kumvera Mulungu ndichinthu chothekakwa anthu opulumutsidwa. Mulungu amalankhula zokhudza khalidwe lachikhristukwa anthu opulumutsidwaokha. Akhristuamayenera kukhala wokhulupirika kwambiri pakukhala m'moyo womvera malamulo a Mulungu. Kunena kuti pamene

tikudikirakubwera kwa Ambuye Yesu, tiyenera kukhala m'moyo wokondweretsa Ambuye.

12. Koma abale, tikupemphani, adziweni iwo amene amagwira ntchito mwa inu, nakhala akulu anu mwa Ambuye, nakuyambirirani inu;
13. Ndipo muwachitire ulemu wapamwambatu mwa chikondi, chifukwa cha ntchito yawo, ndipo khalanindimtendere mwa inu nokha.

Pamene Paulo akunena kuti"adziweni" akunenakuti azindikireni amene amaphunzitsa Mau a Mulungu.Kutanthauza kuti tiyenera kuwalemekeza anthu amene amaphunzitsa Mau a Mulungu. Paulo amapereka lamulo limeneli kwa anthu amene adakhala nawo nthawi pafupifupimwezi umodzi. Mpingo umenewu unali utangoyamba kumene.Pakati pawo panali ena amene anali ndi mphatso yophunzitsa Mau a Mulungu.Ena anali ndi mphatso zopereka ndi ena zachifundo.Mkhristu aliyense amalandira mphatso akapulumutsidwa ndipo mphatso zimenezi zimayenera kugwira ntchito mu mpimgokumangirira thupi la Khristu.

Tsono chifukwa chakuti anthuwa adalandira Yesu nthawi imodzi ndikhulupirira kuti ena mwa iwoamadeleraanzawo. Mwina amaganiza kuti kodi uyu,angandiphunzitse chiyani munthu wakuti tidalandira Yesu nthawi imodzi.Iyeyu tidadziwanakalekale tonse tisanalandireYesu, kodi lero akuganiza kuti akhoza kukhala mphunzitsi wanga? Pachifukwa ichi Paulo akuwapatsa lamulo kuti alemekeze anthu amene ali ndi mphatso zosiyana-siyana pakati pawo. Awazindikirendikuphunzira kuchokera kwa iwo.

Wokondedwa anzanga apaulendo bvuto ili,likadalipo mu mpingo lero. Anthu ena salemekeza anthu amene ali ndi mphatso zotumikira pa mpingo. Anthu ena amanena kuti amakhulupirira kuti Buku Lopatulika ndi Mau a Mulungu.Koma funso nkumati kodibwanji samvera Mau a Mulungu pochita zimene limanena?Chifukwa chiyani sachita zimene Buku Lopatulika limaphunzitsa? Tiyenera kukhala anthu ochita Mau a Mulungu pomvera zimene Buku Lopatulika limaphunzitsa kudzera mwa iwo amene ali ndi mphatso yophunzitsa. Chonchoakhristu pa mpingo adziwe anthu amene Mulungu adawapatsa mphatso

yophunzitsandikulalikiraMau a Mulungu ndikumvera zimene Mau a Mulungu akunena kudzera mwa anthu amenewo.

Lamulo lachinayindilakuti: muwachitire ulemu wapamwambatu mwa chikondi, chifukwa cha ntchito yawo. Atumiki a Mulungu ayenera kulandira ulemu kwa anthu amene amawatumikira. Khalani abwenzi awo, alandireni m'nyumba zanu ngakhale kuti sangakwanitse kukhala mlendo m'nyumba za anthu onse.Kuchitira ulemu atumiki a Mulungu kumawonetsa chikondi cha pa abale.Zimawonetsa kuti anthu akumvera Mau a Mulungu.

Tikunena kuti ntchito yotumikiraatumiki a Mulungu imafunika ulemu.Amene akutumikiramokhulupirika ayenera kulandira ulemu chifukwa cha ntchito yawo.Inu ndi ine tiyenera kuwalemekeza atumiki a Mulungu chifukwa yabwino, yotiphunzitsa Mau a Mulungu ndikuthandiza kuti tisachoke pa njira ya Kumwamba.
Wokondedwa nzanga apaulendo, tikunena kuti inu ndi ine, tiyenera kulemekeza atumikiwa chifukwa cha ntchito yawo yomwe imatichitiraifeubwino. Ntchito yawo imalimbikitsa nzeru, mtendere, kugwira ntchito molimbika, kukhala ndi makhalidwe abwino,

kukhala pa dziko molongosokamopanda chinyengo.Kutsindika kunena kuti ntchito ya utumiki imatitengera pa njira yowongokayopitaKumwamba.Pachifukwa ichi, anthu onse ogwira ntchito yotere ayenera kulandira ulemu.

Lamulo lachisanulikutikhalanindimtendere mwa inu nokha.Pakhale wina amene ali ndi udindo wotsogolera mpingo. Tanthauzoza kuti munthu aliyense sangakhalewotsogolerandipo zinthu sizingayendemwadongosolo labwino.Pachifukwa chimenechi, tiyeni tigwire ntchito limodzi ndi munthu amene ali ndi udindo wotsogolerayo. Tiyenera kulimbikitsanandikutonthozana wina ndi mzake. Tiyenera kuzindikira mphatso zimene Mulungu adaperekakwa wina aliyense. Amene amatiphunzitsa ndi kulalikira mau a Mulungu ayenera kulandira ulemu pakati pathu.Popeza pakutero timalemekeza Mau a Mulungu pochita zimenezi. Tsopano tiyeni tiwone lamulo lachisanu ndi chimodzi mpaka lachisanu ndi chinayi;

14. Ndipo tidandaulira inu abale, yambiriraniamphwayi, limbikitsaniamantha mtima, chilikizaniwofoka, mukhale woleza mtima pa onse.

“Yambiriraniamphwayi”: Lamulo ililikugwirizana kwambiri ndi lamulo lachisanu lakuti “khalani ndi mtendere mwa inu nokha.” Anthu aamphwayi ndi anthu amene afooketsedwa ndimachimo. Anthu otere amakhala odzipatula, ndipo amachita zofuna zawo zokhaosakhalanso ndi mtima wofuna kuchita ntchito ya Mulungu.

Paulo akutchulanso za anthu ‘amantha’ amene timawatchula kuti anthu ofooka mtima.Apasitikukamba za anthu amisala ayi. Awa ndi anthu amene afooka, kotero kuti akulephera kutumikira Mulungu.Anthu awa kusowa chilimbikitso.Alipo ambiri mu mpingo lero adafookandipoakusowa wina wakuti awagwire dzanja ndikuwalimbikitsapaulendowu.Nkhani ikuti aliyense amafooka mtima nthawi ina yake ndipo amafuna mnzake womulimbikitsa.

Ndiye pa lamulo lachisanu ndi chitatu, akunena kuti Chilikizaniwofoka.Akristu enandiwofookam’chikhulupiriro chawo.Awa ndi wofooka chifukwa sadakhwime mu mzimu, akadali ana mu uzimu.Akhristu otere amafunika wina wowachilikiza kuti akhwime.Kutsimikiza kuti inu muyenera kuwanyamulandikuwagwira dzanja kuti angagwe. Pachifukwa

chimenechi, akupereka lamulo lakuti, “Mukhale woleza mtima pa anthu onse: Osakhala anthu opsa mtima msanga.”Alipo mu mpingo anthu amene ndi obvuta kukhala nawo.Zochita zawo zimakhala zofuna kugwetsaanzawo mwanjira zopanda khalidwe.Zimakhala zobvuta ndithu kuleza mtima ndi anthu otere.Koma Mulungu akutilamula kuti tikhale oleza mtima ndi anthu onse ngakhale ndi anthu ochita zopanda pake.

15. Penyani kuti wina asabwezere choyipa womchitira choyipa; komatu nthawi zonse mutsatire chokoma, kwa anzanu, ndi kwa anthu onse.

Tsono lamulo la khumi likuti: ‘Penyani kuti wina asabwezere choyipa womchitira choyipa.’Kutanthauza kuti osachitandeu wina ndi mzake.Dziwani kuti mukuganiza zoyipa mukangokhala ndi mtima ofunakubwezera choyipa kwa wina amene wakuchitirani choyipa. Inde, muyenera kudziteteza, ndikuteteza moyo ndi katundu wanu kapena wa anthu ena koma musachite izi ndi mtima wofunakubwezera choyipa. Kudziteteza kapena kuteteza ena kusankhale kuchokera mu mtima wofunakubwezera choyipa kwa anthu amene akuchitirani choyipa.

Tsono palamulo la khumi ndi chimodzi, Paulo akuti, “Komatu nthawi zonse mutsatire chokoma, kwa anzanu, ndi kwa anthu onse.”Kutanthauza kuti anthu achikunja amachita zinthu zoyipa m’malo mwazinthu zokoma.Iwo, amakhala ndi mtima wodzikonda. Amachita zinthu kuti ziwakomereiwo wokha basi, za munthu wina alibe nazo ntchito. Kutanthauza kuti akunja amachita zinthu zofuna kuti apindule ndiwo wokha basi.

Pamene pali gulu lina limene limachita zinthu zabwino kwa okhawo amene awachitira zabwino. Gulu limeneli limayendera makhalidwe obvomerezeka ndi anthu amene ali pakati pawo. Mwachitsanzo, ngati wina anakuthandizani kupeza udindo ndiye kuti muyenera kumuganizira mwa njira ina yake. Khalidwe ili ndi lachinyengo. Yesu adadzudzula m’chitidwe woterewu pa Luka 6:33 pamene adati: “Ndipo ngati muwachitira zabwino iwo amene akuchitirani inu zabwino, mudzalandira chiyamiko chotani? Pakuti anthu wochimwa amachitansochomwecho?”

Akhristu ayenera kukhala mosiyana ndi makhalidwe a dziko lapansi.Ife, tiyenera kuwachitira zabwino iwo amene atichitira

zoyipa. Munthu wosakhulupirirasangachite zimenezi.Wina atangomuchitira choyipa amafuna abwezere nthawi yomweyo.Kumbukirani kuti mudachoka pakati pa osakhulupirirawo ndipo nthawi zonse mutsatire chokoma kwa anzanu komanso kwa anthu onse.

Tsopano lamulo lakhumi ndi chiwiri likuti;"Kondwerani nthawi zonse."Mau akuti kondwerani sakutanthauza kuti 'sangalalani.'Paulo akugwiritsa mau akuti kondweranimonga momweadagwiritsam'kalata yake kwa Afilipi pamene adalemba kuti "kondwerani nthawi zonse, ndipo ndinenansokondwerani." Ana a Mulungu akulamulidwakuyendaali wokondwera nthawi zonse. Wokondedwa anzanga apaulendo, kukondwera uku ndichipatso cha Mzimu Woyera.Kutanthauza kuti inu ndi ine, tiyenera kuyenda ndi wodzadzidwa ndi Mzimu Woyera amene amatipatsa chimwemwe ndi mtendere mu mtima.Chipatso cha Mzimu woyera ndicho chikondi, chimwemwe, mtendere-ngati mulibe chimwemwe yambani kuwerenga Mau a Mulungu ndikupempha Mulungu kuti akupatseni chimwemwe mumtima.Mulungu ndiye ameneamapereka chimwemwe!

16. Pempherani kosalekeza.

Lamulo ili,silikutanthauza kuti tikhale pamaondo athu ndikupemphera tsiku lonse nthawi zonse ayi. Koma mkhristu ayenera kukhala ndi nyengo yopempherapayekha, ndi banja lake, komanso ndi onse amene amayitanira pa dzina la Ambuye. Nthawi yopempheraikhale nthawi yokhazikikayosasokonezedwa mwachisawawa.

Kutsindika kuti tiyenera kukhala ndi nthawi yopemphera kaya tapemphedwa pagulu, kaya mseripatokha, tizikhala ndi mtima wosafokakupemphera.Nkhani ikuti mkhristuamafowoka ndipo amalepherakupemphera chifukwa cha zinthu zapadziko, kapena chifukwa chowerenga mabuku oyipa. Moyo wa munthu amene sayanjana ndi Mulungu popempheraamakanikakuyandikira ku mpando wachifumu mwapemphero.

18. M'zonseyamikani: pakuti ichi ndichifuniro cha Mulungu cha kwa inu, mwa Khristu Yesu.

Pano tikulamulidwa kukhala woyamika mu zinthu zonse.Osangoyamikakamodzi pa chaka kapena pamene zinthu

zikuwoneka kuti zatiyendera bwino koma tikhale woyamika nthawi zonse.Tikhale woyamika nthawi zonse chifukwa ndi chifuniro cha Mulungu pa moyo wathu. Chifuniro cha Mulungu ndi chakuti: kondwerani nthawi zonse, pempherani kosalekeza komanso yamikani mu zinthu zonse.

19.MusazimeMzimuyo.

Mzimu Woyera umafanizidwa ndi moto. Funso nkumati: kodi moto umazima bwanji? Moto umazima pamene wathiridwa madzi komanso osaukolezera.Kuzima Mzimu ndikukhala moyo wosafuna kuchita chifuniro cha Mulungu.Munthu amene sakuchita chifuniro cha Mulungu amakhala munthu osamvera Mzimu Woyera.Munthu wotere safuna kutsogozedwa ndi Mzimu Woyera.Timazimitsa Mzimu Woyera tikachita zinthu monga mwachifuniro chathu, kungotsatira maganizo athu.Paulo adaphunzitsaakhristu aku Aefeso 4:30, mofanana pamene adati: "Ndipo musamvetse chisoni Mzimu Woyera wa Mulungu, amene mudasindikizidwachizindikiro mwa Iye, kufikira tsiku la mawomboledwe." Mzimu Woyera amamva chisoni ndi wokhulupirira amene akuyenda mu tchimo.Mzimu Woyera amazima pamene munthu okhulupiriraachokam'chifuniro cha Mulungu.

20. Musanyozemanenero.

Nkhani ikuti inu simuyenera kunyoza maphunziro a Mau a Mulungu ngati chinthu chopanda phindu.Pali anthu ambiri amene amatumikiram'mabungweosiyanasiyanaachikhristu, ndiposasamala Mau a Mulungu.Ambiri amaganiza kuti kuphunzira Mau a Mulungu ndikutaya nthawi.Anthu ena amaganiza kuti timayenera kukhala achangu kutumikira osamangochedwandikuphunzira Mau a Mulungu.Zoonadi ndi zakuti munthu sungatumikiremoyenera pokhapokha anaphunzirakutumukira monga mwa Mau a Mulungu. Nkhani ikuti anthu amene amathamangira utumiki osaphunzira Mau a Mulungu satumikirakwa nthawi yaitali. Ambiri mwa anthu otere amasiya kutumikira atakhumudwa ndi zosiyanasiyana koma nkhani yayikulu imakhala yakuti samayikira Mau a Mulungu ku mtima.Ichi, ndichifukwa chake Paulo akunena kuti, "musanyozemanenero" kutanthauzakuti musanyoze Mau a Mulungu.Kodi inu mumaika mtima wanu pa mau a Mulungu?

21. Yesani zinthu zonse; sunganichokomacho.

Ili, ndilamulo lomwe likunena kuti, osamangotengeka ndi zinthu ziri zonse.Kunja kuno kuli chinyengo chambiri.Taonani anthu ena amakhala ngati akuthandiza ana amasiye, koma pamene

akuwabera.Tikunena kuti inu simuyenera kukhala munthu opusitsidwamosabvuta, muyenera kukhalaniochenjerapoyesa zinthu zonse.

Tsono kuti mupambane muyenera kuyesa zinthu zonse.Chinthu chirichonse chimene mwamva mwa uneneri kapena ulalikichiyeseni ndi Mau a Mulungu.Uneneri kapena ulaliki uliwonse uyenera kugwirizana ndi Mau a Mulungu.Ndipo zirizonse zimene zikugwirizana ndi Mau a Mulungu zimenezo ndiye zokoma.Tikunenetsa kuti uneneri ungakome bwanji m'makutu athu ngati sugwirizana ndi Mau a Mulungu, Inu, simuyenerakusungachimenechi.Uneneri uyenera kukulitsa chikhulupiriro, chikondi ndi chiyero.

22. Mupewemawonekedwe onse a choyipa.

Ili, ndilamulo lomwelikukhudza zinthu zosangalatsa moyo.Pamene inu muli ndi chikayiko kuti chinthucho ndi chabwino kapena choyipa, muyenera kupewa chinthu chimenecho.Pewani kalikonse kamene kali koyipa ngakhale kalikonse kamene kali nawo mawonekedwe chabe.

Pali zinthu zina zimene zimadziwikiratu kuti ndi zoyipa komanso zinthu zimene zikukayikitsanazonsopewani ndithu. Zinthu izi zikukhudza zinthu zambiri monga;mabvalidwe, zinthu zachisangalalo ngati mabvinidwe ndi magule oipa,ngakhalenso kachitidweka malonda ngati zonsezi zili ndi mawonekedwe a choyipa pewani. Pa zinthu zotere mudzakhala ndi chitsimikizo mumtima mwanu kuti simunatengepo gawo la uchimo mukapewa.

23. Ndipo Mulungu wa mtendere yekha ayeretse inu konse konse; ndipo mzimu wanu ndi moyo wanu ndi thupi lanu zisungidwezamphumphu, zopanda chilema pa kudza kwake kwa Ambuye wathu Yesu Khristu.

Munthu ali ndi thupi, malingaliro (moyo) ndi mzimu. Magawo onsewa asowa kukhala oyeretsedwa ndi Mulungu kufikira titafikapokhwimandi kukhala wamphumphu.Kunena kuti sitingakhale ngati makanda moyo wathu onse komatikuyenerakukula.

24. Wakuyitana inu ali wokhulupirika, amenensoadzachichita.

Mulungu ndiwodalilikakutanthauza kuti chiyero chathu chimachokera kwa Mulungu amene adayamba ntchito imeneyi

m’mitimamwathu ndipo tidalire Mulungu yemweyo kuti adzayitsiriza.

25. Abale, tipemphererereniife.

Pemphoili Mtumwi Paulo amapemphapafupipafupi. Ndipo lero sitingapempheremtumwi Paulo, koma tiyenera kupempherera atumiki athu.Ili, ndilamulo lomwe likupezeka pa Ahebri 13:18 pamene akuti: “Mutipemphererereife; pakuti takopeka mtima kuti tiri nacho chikumbumtima chokoma m’zonse, pofuna kukhala nawo makhalidwe abwino.”Mtumiki ndi munthu ngati ife tomwe ndipo amakumana ndi mayeseroosiyansiyana. Atumiki amakumana ndi zipsinjo zambiri ndipo amayenda mu zinthu zowopsapafupipafupi.Pachifukwa ichi tiyenera kuwapempherera atumiki athu.Anthu amene amapempherera atumiki awo amatumikiridwamoyenera.Kodi inu, mumawakumbukira atumiki kapena abusa anu?

26. Patsani moni abale onse ndi chipsompsonochopatulika.

Ilinso ndi lamulo lomwe likuchenjezakuti musalonjerane ngati anthu akunja.Pakhalechiyeropolonjerana wina ndi mzake.

27. Ndikulamurirani mwa Ambuye kuti kalatayuawerengedwekwa abale onse woyera mtima.

Ili ndi lamulo la 22. Limeneli ndi lamulo lochokerakwa Ambuye osati pempho chabe ayi. Kalataayiimayenerakuwerengedewa ndi abale onse ku Atesalonika osati anthu ena osankhikaokha ayi.Kutsindika kuti munthu aliyense ayenera kukhala ndi mwayi wa Mau a Mulungu. Pasakhale anthu ena amene aziwerenga Mau a Mulungu ndikumabisila anthu ena Mau a Mulungu.Mau a Mulungu ayenera kuwerengedwa pagulu la anthu onse komanso anthu akhale ndi mpatawowerenga Mau a Mulungu pawokhapawokha.Ndipo Paulo akumaliza ndi m'dalitso.Pamene akupemphera kuti chisomo cha Ambuye Yesu Khristuchikhale ndi wokondedwa onse mwa Kristu.

Lero tilekeza pano. Ndipo timasanthula 1 Atesalonika 5:11-28, m'mene timaona za malamulo ya akristu.

Ambuye akudalitseni inu. Amen!